KODI

# NDONDOMEKO YA KUKWEZA NTCHITO ZA MALIMIDWE (GREEN REVOLUTION) MU AFRICA

## NDI CHANI?




duducoelho.com

Ndondomeko ya Kukweza Ntchito za Malimidwe (Green Revolution) imayimila ntchito yopanga mitundu ya mbeu zimene zimapatsa mochuluka, zimene zimatchedwanso kut 'zamakono' kapena kuti 'zovomelezeka'. Mitundu iyi ya mbeu imapangidwa makamaka ndi cholinga chopatsa zokolola zochuluka pa hekitala, ngati gawo limodzi a zipangizo m'mene muli foteleza omwe si wachilengedwe, mankhwala ophela tizilombo komanso mankhwala ena ndi ena, ndalama zoyendetsela ntchito za malimidwe, komanso kupeza misika yogulitsako mbeu, ndi zina zotelo.

Olimbikitsa ndondomeko za Kukweza Ntchito za Malimidwe amanena kuti njila zawo zimalimbikitsa bwino ulimi wokhazikika, komanso chakudya chokwanira ndi chamagulu wonse woyenelera mthupi. Nzeru zawo zili pakuti alimi azigula zipangizo (zimene zikhoza kukhala zotsika mtengo kwa nyengo za mvula zochepa zoyambilira ngati poyambira), zimene zingawapangitse kukolola zochuluka zomwe zikhoza kugulitsidwa kuti apeze phindu. Izi zikhoza kubweletsa cholowa chokwanila chimene chikhoza kufikila kugula zofunikila zokhudzana ndi chakudya kufikila nyengo ine ya mvula komanso kugula zipangizo za ulimi.

**Kunena zoona, izi siziyenda chonchi, ndipo ndi gawo lochepa chabe la alimi amene angapindule kuchokela ku njira imeneyi.**

www.acbio.org.za info@acbio.org.za Tel +27 (0)11 486 1156

african centre for biodiversity